Zimene Mungachite Mukalakwitsa Zinthu

Mafunso amene ali m'munsiwa akuthandizani kuona (1) zimene mumakonda kuchita mukalakwitsa zinthu ndi (2) zimene zingakuthandizeni kuti muzichita zinthu mwanzeru mukalakwitsa zinthu.

Kodi inuyo mukuganiza bwanji?

1 N'chifukwa chiyani achinyamata ena savomereza zimene alakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

.....

.....

CHITSANZO: "Sindivutika kuvomereza mumtima mwanga kuti ndalakwitsa zinazake, koma zimandivuta kuvomereza pamaso pa anthu kuti ndalakwitsa. Sindifuna kuti anthu azindiona molakwika."—Melinda.

2 Kodi mukuona kuti anthu angamaganize zotani zokhudza inuyo ngati nthawi zonse simuvomereza mukalakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

.....

.....

CHITSANZO: "Mbiri yako imaipa ngati ukalakwitsa zinazake umakana kuvomereza kuti walakwitsa. Anthu amatha kumvetsa munthu akalakwitsa koma sasangalala ndi munthu wachinyengo."—Christine.

3 Kodi anthu angamakuoneni kuti ndinu munthu wotani ngati mumavomereza moona mtima zimene mwalakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

.....

.....

CHITSANZO: "Ndikukumbukira nthawi zingapo pamene ndinavomereza kuti ndalakwitsa. M'malo mondinyoza, anthu anandilemekeza kwambiri."—Richard.

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kodi *muyenera* kuchita chiyani?

Munabwereka njinga ya bambo anu ndipo mwaiwononga.

- ☐ Osanena chilichonse poganiza kuti bambo anu sadziwa.
- ☐ Kuwauza zimene zinachitikadi.
- ☐ Kuwauza zimene zinachitika koma n'kunena kuti munthu wina ndi amene analakwitsa.

Tiyerekeze kuti mukusewera mpira ndipo mwangozi mpirawo waswa galasi la windo la nyumba ya aneba anu.

- ☐ Kungothawa.
- ☐ Kuuza eni nyumbayo kuti mwaswa galasi la windo lawo ndipo mulipira.
- ☐ Kunamizira munthu wina.

Tiyerekeze kuti mwalephera mayeso chifukwa chakuti simunkawerenga.

- ☐ Kunena kuti mayesowo anali ovuta.
- ☐ Kuvomereza kuti mwalephera mayesowo chifukwa chakuti simunkawerenga.
- ☐ Kunena kuti aphunzitsi anu amadana nanu choncho akulepheretsani.

Tsopano ganiziraninso zitsanzo zitatuzi ndipo muyerekeze kuti ndinu (1) bambo anu, (2) aneba anu, komanso (3) aphunzitsi anu.

Kodi bambo anu, anthu amene mumakhala nawo pafupi komanso aphunzitsi anu akanaona kuti ndinu munthu wotani mukanakhala kuti mwavomereza zimene mwalakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

Kodi akanaganiza kuti ndinu munthu wotani mukanakhala kuti mwanamizira munthu wina kapena mwabisa zimene mwalakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tchulani chinthu chimodzi chimene munalakwitsa chaka chathachi.

Kodi munalakwitsa chiyani?

.....

.....

.....

Kodi munachita chiyani mutazindikira kuti mwalakwitsa?

- ☐ Sindinanene chilichonse.
- ☐ Ndinanamizira munthu wina.
- ☐ Ndinaulula zimene ndinalakwitsa.

Ngati **simunavomereze** kuti mwalakwitsa, kodi munamva bwanji pamapeto pake?

- ☐ Ndinasangalala chifukwa palibe anadziwa.
- ☐ Ndinakhumudwa chifukwa ndinaona kuti ndinayenera kuulula.

Kodi mukuona kuti ndi njira yabwino iti imene mukanatsatira?

.....

.....

.....

.....

.....

Kodi munaphunzira chiyani pa zimene munalakwitsa?

.....

.....

.....

.....

.....

M'miyezi 12 ikubwerayi, kodi mungakonze mfundo zotani zoti muzitsatira zimene zingakuthandizeni kuti muzichita zinthu mwanzeru mukalakwitsa zinazake?

.....

.....

.....

.....

.....

Werengani nkhani zina zimene zingakuthandizeni.

Kuti mudziwe zambiri pa nkhani yokhudza kuvomereza mukalakwitsa zinthu, werengani lemba la 2 Samueli 12:1-13 kuti mudziwe zimene Davide anachita atalakwitsa zinthu. Kenako yerekezerani zimenezi ndi nkhani yopezeka pa 1 Samueli 15:10-26 yofotokoza zimene Sauli anachita atalakwitsa zinthu.

Kenako ganizirani izi: Davide komanso Sauli sanavomere **nthawi yomweyo** zimene analakwitsa ngakhale kuti **patapita nthawi** onse anavomera. Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Yehova Mulungu anakhululukira Davide koma sanakhululukire Sauli?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania